-Dzina lakuti Isilayeli likutanthawuza kuti kulimbana ndi Mulungu.



# PHUNZIRO LA 23

1. Kodi zanatheka bwanji Abulahamu, amene anali ndi zaka 100, ndi Sara amene anali ndi zaka 90 ndipo osabereka, kukhala ndi mwana wamamuna?

-Chifukwa chakuti ndi Mulungu amene amapereka moyo.
-Chifukwa chakuti Mulungu angathe kuchita china chilichonse.

2. Kodi Abulahamu anamutcha mwana amene Mulungu anamupatsayo dzina lakuti ndani?
-Isaki.

3. Kodi Abulahamu ndi sara amkadziwa zakuti Mulungu anakonza zotumiza Mpulumutsi kupitira mu m'bado wa Isaki?
-Inde.

4. Kodi zinatheka bwanji kuti Mulungu amulamule Abulahamu kuti amupereke Isaki ngati msembe yopsereza?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamupatsa moyo Abulahamu.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamupatsa moyo Isaki.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi AMBUYEwa anthu onse.

5. Mulungu anamuwuza Abulahamu kuti Isaki adzakhala ndi zidzukulu zambiri, ndipo Mpulumutsi adzakhala chidzukulu chake. Kodi Mulungu anasintha maganizo Ake?
-Iyayi.

6. Kodi Abulahamu amkaganiza kuti Mulungu wasintha maganizo Ake?
-Iyayi.

-Abulahamu amkakhulupilira mwa Mulungu ndi malonjezo Ake.

7. Kodi Abulahamu amkakhulupilira kuti Mulungu adzachita chiyani iye akamupereka Isaki ngati msembe?
- Mulungu adzamudzutsa Isakiyo kuchokera kwa akufa.

8. Kodi Abulahamu anakatha kumupulumutsa Isaki?
-Iyayi.

9. Kodi chifukwa chiyani Abulahamu sanakatha kumupulumutsa Isaki?
-Chifukwa chakuti Abulahamu anali atanyamula kale dzanja lake kuti amuphe Isaki ndikumupereka ngati msembe.

10.Kodi Isaki anakatha kudzipulumutsa yekha?
-Iyayi.

11. Kodi chifukwa chiyani Isaki sanakatha kudzipulumutsa yekha?
-Chifukwa chakuti Abulahamu anamanga manja ndi miyendo ya Isaki.

12. Kodi anthu ena angathe kutipulumutsa ife?
-Iyayi.

13. Kodi Ife tingathe kudzipulumutsa tokha?
-Iyayi.

14. Kodi ndani yekha amene angathe kutipulumutsa ife?
-Mulungu.

15. Kodi ndani amene analankhula kwa Abulahamu ndikumupulumutsa Isaki?
-Mulungu.



-Yakobo anakhala zaka zambiri ku Harani.

-Ku halani, Yakobo anakwatira munthu ndi mphwake, ndipo anabereka ana amuna 12.

-Yakobo atakhala ku Harani kwa zaka zambiri, Mulungu analankhulanso kwa iye.

-Apa pali zimene analankhula Mulungu kwa Yakobo akukhalabe ku Harani.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 31:13

13-[Mulungu anati], "Ine ndine Mulungu amene ndinakuwonekera ku Betele kuja kumene udayimika mwala wa chikumbutso ndi kuwudzoza mafuta, ndipo kumeneko unalumbira kea Ine. Konzeka tsopano uchoke kuno, ubwerere ku dziko la kwanu."

-Yakobo atakhala ku Harani kwa zaka zambiri, kodi Mulungu anamuwuza chiyani Yakobo?

-Mulungu anamuwuza Yakobo kuti achoke ku Harani ndipo abwere ku dziko la kwawo.ku Kanani.

-Pamene Yakobo amkabwerera kwawo ku Kanani, Mulungu anamupatsa iye dzina latsopano.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 32:28

28-Kenako [AMBUYE] anati, "Dzina lako silidzakhalanso Yakobo, koma Isilayeli."

-Mulungu anamupatsa Yakobo dzina latsopano.
-Dzina latsopano la Yakobo linali Isilayeli.

-Tsopano Mulungu amkamupatsa Yakobo malonjezo amene anaŵapereka kwa Abulahamu ndi Isaki.

-Kodi Mulungu anamulonjeza chiyani Yakobo?

-Mulungu anamulonjeza Yakobo kuti adzakhala ndi zidzukulu zambiri.
-Mulungu analonjeza kuti adzamudalitsa Yakobo.

-Mulungu analonjeza zoŵadalitsa anthu onse poŵatumizira Mpulumutsi, amene adzakhale chimodzi mwa zidzukulu za Yakobo.

-Kodi Mulungu analiyiŵala lonjezo Lake lotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.
-Mulungu sangaliyiwale lonjezo Lake lotumiza Mpulumutsi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sangaliyiwale lonjezo Lake lotumiza Mpulumutsi?

-Chifukwa chakuti Mulungu sangayiwale.
-Chifukwa chakuti Mulungu sangasinthe.
-Chifukwa chakuti nthaŵI zonse Mulungu amasunga Malonjezo Ake.

-M'mawa mwake, Yakobo anapitiliza ulendo wake.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 29:1

1-Chomcho Yakobo anapitiliza ulendo wake, kupita ku dziko la anthu a ku vuma.

-Yakobo anapitiliza ulendo wake mpaka anakafika ku dziko la Harani.



16. Kodi ndani amene anapereka msembe yolowa m'malo mwa Isaki?
-Mulungu.

17. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamumanga mwana wa nkhosa ndi nyanga zake?
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti alandire msembe yabwino kwambiri m'malo mwa Isaki.

18.Kodi chifukwa chiyani Abulahamu anaŵatcha malowo kuti, "AMBUYE adzapereka?"

-Abulahamu amkakhulupilira kuti tsiku lina Mulungu adzapereka Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu ngati m'mene Iye anaperekera mwana wa nkhosa kudzamupulumutsa Isaki.

-Mkazi wa abulahamu, Sara, anakalamba ndipo anamwalira.

-Isaki anaŵalilira mayi ake kwa nthaŵI yayitali, koma atate ake anamutonthoza pomupatsa iye mkazi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 24:67; 25:20

67- Chomcho Isaki anatenga Rabeka kuti akhale mkazi wake naloŵa naye m'hema mwake. Isaki anamukonda kwambiri Rabekayo, mwakuti zimenezi zinamutonthoza pa imfa ya mayi ake ija.
20- Ndipo pamene Isaki anakwatira Rabeka mkuti ali wa zaka makumi anayi.

-Dzina la mkazi wa Isaki linali Rabeka.
-Rabeka anabadwira ku dziko limene Abulahamu amkakhala kale Mulungu asamutsogolele iyekupita ku Kenani.

-Patapita nthaŵI, Abulahamu nayenso anamwalira.

-Chifukwa chakuti Rabeka,  mkazi wake wa Isaki anali osabereka, iwo analibe ana.

-Koma Isaki anamupempherera iye, ndipo Mulungu anamuyankha pemphero lake.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 25:21-23

21-Chifukwa chakuti Rabeka anali osabereka, Isaki anamupempherera Rabekayo amene anali mkazi wake kwa AMBUYE. AMBUYE anamva pemphero lake, ndipo Rabeka anatenga pathupi.
22-Koma pamene ana aŵiriwo anayamba kulimbana m'mimba mwake, adati, "Ngati umu ndi m'mene zikhalire zinthu, ndikhaliranji ndi moyo?" Ndipo anakafumsa AMBUYE kuti  amuyankhe.
23-AMBUYE anamuwuza kuti , "M'mimba mwakomo muli mitundu iŵiri ya anthu. Udzabereka mafuko a anthu olimbana: mwana wina adzakhala wa mphamvu kupambana nzake, wamkulu adzakhala wotumikira wamng'ono."

-Ana a Rabeka asanabadwe, Iye anaŵafunsa AMBUYE za anawo.

-Kodi AMBUYE anayankha kuti chiyani?
-AMBUYE anayankha kuti Rabeka adzabereka ana a mapasa, ndipo wamkulu adzidzamutumikira wamng'ono.

-Ana a Rabeka asanabadwe, Mulungu anali atadziŵa kale za anawo.

-Kodi Mulungu anazidziŵa bwanji zonse za ana a Rabekawo asanabadwe?
-Mulungu amazidziŵa zonse za anthu onse.



-Ndipo Mulungu analonjeza zodzatumiza Mpulumutsi amene adzaŵabweretsenso anthu ndi Mulungu pamodzi.

-Mpulumutsi ndi njira yokhayo yokafikira kumwamba ngati m'mene makwelero analili niira yokhayo yokafikira kumwamba.

-Mulungu anayankhula kwa Yakobo m'maloto ake.

-Apa pali zimene Mulungu anayankhula kwa Yakobo m'maloto akewo:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 28:13b-15

13-[Mulungu] anati: "Ine Ndine AMBUYE, Mulungu wa Abulahamu ndi Isaki. Dziko limene ukugonali ndidzakupatsa iwe pamodzi ndi zidzukulu zako.

14-Zidzukulu zakozo zidzachulukana ngati fumbi la pa dziko la pansi, zidzabalarikira  ku zambwe, Ku vuma, ku mpoto ndi ku mwera. Ndipo mitundu yonse ya pa dziko la pansi idzadalitsidwa kudzera mwa iwe ndi zidzukulu zako.
15-Ndili nawe, ndipo ndidzakutchinjiriza kulikonse kumene udzapite, ndipo ndidzakubweretsanso ku dziko lino. Sindidzakusiya mpaka nditachita zonse zimene ndakulonjezazi."

-Kalekale, Mulungu amkalankhula ndi anthu m'maloto.

-Kodi masiku ano Mulungu amalankhula bwanji ndi anthu?
-Masiku ano, Mulungu amalankhula ndi anthu kupitila mu Buku Lake.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analankhula kwa Yakobo?
-Mulungu amkapereka malonjezo kwa Yakobo.

anakabweleranso kwa Mulungu.

-Koma Mulungu analonjeza zotumiza Mpulumutsi, amene adzaŵabweretsenso anthu a pa dziko la pansi ndi Mulungu wa Kumwamba pamodzi.

-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu, kuti anthuwo ndi Mulungu adzidzayenderanso pamodzi.

-Apa pali chitsanzo:

-Patiliki ndi Yosefe anali pa ubwenzi.
-Anali ndi mdani wawo.
-Mdani wawoyo amkawuchitila msanje ubwenzi wawowo.

-Tsiku lina mdani wawoyo anaganizira za njira yowonongera ubwenzi wa Patiliki ndi Yosefe..

-Mdaniyo anapita kwa Patiliki ndipo anamuwuza kuti, Yosefe akufuna kumuvulaza iye.

-Patiliki analikhulupilira bodza la mdaniyo; ndipo anasiyana ndi nzake, Yosefe.

-Koma Yosefe amkamukondabe Patiliki, ndipo anaganiza za njira yowubwezeretsanso ubwenzi wawo uja.

-Yosefe anamutumiza mwana wake kuti akalankhule ndi Patiliki, ndipo akamuwuze kuti mdani wawo wamunamiza iyeyo.

-Chifukwa cha mwanayo, Yosefe ndi Patiliki anabwereranso pa ubwenzi.

-Satana anamunamiza Adamu ndi Hava, ndipo anasiyana ndi Mulungu.



-Palibe chobisika kwa Mulungu.

-Ufe tisanabadwe, Mulungu amakhala atazidziŵa kale zonse za ife.

-Mulungu amazidziŵa zonse zimene zinatichitikira ife kalekale.
-Mulungu amazidziŵa zonse zimene zikuchitika kwa ife tsopano.
-Mulungu amazidziŵa zonse zimene zidzatichitikire ife mtsogolo.

-Patapita nthaŵI, Rabeka anabereka ana aŵiri a mapasa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 25:24-26

24-NthaŵI yakuti achire itakwanira, Rabeka anabereka mapasa.
25-Mwana woyamba kubadwa anali ofira, ndipo thupi lake lonse linali ngati chovala cha ubweya. Chomcho anamutcha kuti Esau.
26-Mng'ona wake pobadwa, dzanja lake linali litagwira chidendene cha Esau. Chomcho anamutcha kuti Yakobo.

-Rabeka anabereka ana aŵili amuna a mapasa.
-Mayina awo anali Esau ndi Yakobo.

-Esau anali oyamba kubadwa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 25:27a

27a-Esau anasanduka mlenje wodziŵa kusaka nyama, wokonda kuyendayenda.

-Esau anali odziŵa kusaka kwambiri, ndipo nthaŵI zambiri

amkakonda kusaka nyama.

-Koma Esau samkakhulupilira mwa Mulungu.

-Yakobo anali wachiŵiri kubadwa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 25:27b

27b-Koma Yakobo anali wachete, wokonda kukhala panyumba.

-Yakobo amkaweta nkhosa ndi ng'ombe.ndipo amkakonda kukhala chete mu hema lake.

-Yakobo amkakhulupilira mwa Mulungu.

-Tsiku lina, china chake chinachitika pakati pa Esau ndi Yakobo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 25:29-34

29-Tsiku lina Yakobo anaphika nyemba zofiira, Esau anabwera kuchokera ku thengo.
30-Anali ndi njala zedi, chomcho anamuwuza Yakobo kuti, "Ine njala yandikola kwambiri! Ndigayileko nyemba zofiira waphikazi!"
31-Koma Yakobo anayankha kuti, "Uyambe wandipatsa ukulu wako wa uchisamba, ndiye ndikupatsa zimenezi."
32-Esau anati, "Chabwino, ine ndili pafupi kufa. Kodi ukulu wangawu, udzandipindulira chiyani?"
33-Yakobo anati, "Uyambe walumbira kuti ukulu wakowu wandipatsadi."Apo Esau analumbira, nagulitsa ukulu wake wa uchisamba kwa Yakobo.
34-Kenako Yakobo anamupatsa Esau mkate pamodzi ndi nyemba zija, ndipo Esau anadya namwera,



amkakhuza pasi ndi kumwamba?
-Makwelerowo amkalilumikiza dziko la pansi ndi kumwamba.

-Kodi amene anali pamwamba pa makwelerowo anali ndani?
-Mulungu.

-Kodi amene amkatsika ndi kumakwera pa makweleropo ndani?
-Angelo.

-Kodi zimkatanthawuza chiyani zakuti angelo amkatsika ndi kumakwera pa makweleropo?
-Mulungu amkafuna kuti akhale Mulungu wa Yakobo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupatsa maloto Yakobo?
-Mulungu amkamuphunzitsa Yakobo za Mpulumutsi amene amkabwera.

-Kodi Mulungu amkamuphunzitsa chiyani Yakobo za Mpulumutsi amene amkabwerayo?

-Ngati m'mene Makwelero amkalilumikizira dziko la pansi ndi kumwamba pamodzi, Mulungu adzatumiza Mpulumutsi amene adzaŵabweretse anthu a pa dziko la pansi ndi Mulungu wa kumwamba pamodzi.

-Pachiyambi, Mulungu amkayenda limodzi ndi Adamu ndi Hava.

-Koma Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, ndipo iwo anasiyana ndi Mulungu.

-Panalibenso njira ina iliyonse yakuti Adamu ndi Hava

-Ku Harani ndi ku dziko kumene anabadwira mayi ake a Yakobo, Rabeka.

-Ku Harani ndi ku dziko kumene agogo ake a Yakobo, Abulahamu, amkakhala Mulungu asanamutsogorere kupita ku Kanani.

-Chifukwa chakuti ku Harani kunali kutali, Yakobo anatha masiku ambiri akuyenda.

-Tsiku lina, Yakobo akugona, Mulungu anamupatsa iye maloto.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 28:10-13a

10-Yakobo ananyamuka ulendo kuchokera ku Beer-eseba, kupita ku Harani.
11-Atafika pa malo pena, anayima pamenepo chifukwa chakuti dzuŵa linali litalowa. Anagona pomwepo ndipo anatsamira mwala.
12-Ndipo analota akuwona makwelero achokera pansi mpaka kukafika kumwamba. Angelo a Mulungu amkatsika ndi kumakwera pa makwelerowo.
13-AMBUYE anayimilira pa mwamba pake.

-Kodi Yakobo anawona chiyani m'maloto akewo?
-Yakobo anaŵawona makwelero.

-Kodi pasi pa makwelerowo panakhuza kuti?
-Pasi pa makwelerowo panakhuza pa dziko la pasi.

-Kodi kumwamba kwa makwelerowo kumkakhuza kuti?
-Kumwamba kwa makwelerowo kumkakhuza kamwamba.

-Kodi zimkatanthawuza chiyani zakuti makwelerowo



Kenako ananyamuka ndikuchokapo. Chomcho Esau adawunyoza ukulu wake wa uchisamba.

-Tsiku lina, Esau Anabwera kuchokera kukasaka nyama ndipo anali ndipo njala kwambiri.

-Esau anamuwona yakobo akuphika nyemba zofiira, ndipo anamulamula Yakoboyo kuti amugayileko.

-Chifukwa chakuti Esau anali ndi njala kwambiri, iye anagulitsa ukulu wale wa uchisamba kwa Yakobo ndi nyemba zofiira.

-Kodi chifukwa chiyani Esau anagulitsa ukulu wake wa uchisamba?
-Chifukwa chakuti samkawugwiritsira tchito ukuluwo.

-Kodi chimene Esau amkachigwiritsira tchito kwambiri ndi chiyani?

-Esau amkayigwiritsira ntchito kwambiri mimba yake.
-Esau amkaligwiritsira ntchito kwambiri thupi lake.

-Kodi Esau ndi Yakobo amkasiyana bwanji?

-Esau samkaganiza kuti anabadwira mu tchimo.
-Yakobo amkadziŵa kuti anabadwira mu tchimo.

-Esau samkaganiza zakuti iye wamuchimwira Mulungu.
-Yakobo amkadziŵa kuti iye wamuchimwira mulungu.

-Esau samkaganiza zakuti tchimo limabweretsa imfa yosatha.
-Yakobo amkadziŵa kuti imfa imabweretsa imfa yosatha.

-Esau samkafuna kumutsatira Mulungu.

-Yakobo amkafuna kumutsatira Mulungu.

-Esau samkafuna kuti Mulungu atumize Mpulumutsi kud-zamupulumutsa iye.
-Yakobo amkafuna kuti Mulungu atumize Mpulumitsi kud-zamupulumutsa iye.

-Ngati munthu woyamba kubadwa, ukulu wa uchisamba unali wa Esau.
-Ngati munthu oyamba kubadwa, Mulungu anakatha ku-tumiza Mpulumutsi kupitira mwa zidzukulu zake.

-Koma Esau samkawugwiritsira ntchito ukulu wake.
-Esau samkafuna kuti Mulungu atumize Mpulumutsi kupiti-ra mwa zidzukulu zake.

-Esau amkangofuna nyemba zofiira zija.
-Esau amkangofuna zimene mimba yake yimkamuwuza iye.

-Kodi ife timachita zimene mimba zathu zimatuwuza?
-Kodi ife timachita zimene thupi lathu limatiwuza?

-Kapena timachita zimene Mulungu watiwuza ife?

-Tikazitsata mimba zathu, zidzatitengera ife ku imfa.
-Tikaŵatsata matupi athu, atitengera ife ku imfa.

-Tikamutsata Mulungu, atitsogolera ku moyo.

-Chifukwa chakuti Esau samkakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anamusankha Yakobo.
-Chifukwa chakuti Esau samkakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anasankha zotumiza Mpulumutsi kupitira kupitira mwa zidzukulu za yakobo.



-Chifukwa chakuti Esau samkakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anapereka ukulu wa uchisamba kwa Yakobo.

-Mulungu atapereka ukulu wa uchisamba kwa Yakobo, Esau anakwiya kwambiri.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 27:41

41-Chomcho Esau anadana naye Yakobo chifukwa chakuti m’malo momudalitsa iyeyo, bambo ake anamudalitsa Yakobo. Ndipo anati, “NthaŵI yakuti ndilire maliro a bambo anga ili pafupi, pamenepo ndidzamupha Yakoboyu.”

-Esau anakwiya kwambiri ndi Yakobo ndipo anakonza zomupha Yakobo.

-Koma mayi ake a Yakobo anamva kuti Esau akufuna ku-mupha Yakobo.

-Chomcho Rabeka anamuyitana Yakobo kuti amutumize ku dziko kumene anabadwira mayi akewo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 27:42-44

42-Koma Rabeka atamva za maganizo onse a Esau, anamuyitana Yakobo ndipo anamuwuza kuti, “Taona, mbale wako, Esau akuganiza zakuti akuphe kuti akulipsire.
43-Tsopano mwana wanga uchite zimene ndikuwuze. Konzeka, thaŵira kwa mulongo wanga, Labani ku Harani.
44-Ubakakhala kwa ameneyo kwa kanthaŵI ndithu mpaka mtima wake atakhalanso pansi.

-Yakobo anaŵasiya mayi ndi bambo ake, ndipo anayamba kuyenda kupita ku dziko la Harani.